


KUTULUKA DZUWA KWA ISITARA

 . . .ndi misonzi, anatulukira akusangalala. Ameni. Oh, pakuti Ine ndiri moyo inunso mudzakhala moyo. Oh mai, ngati oyer a Chipangano Chakale amakhoza kuganiza zimenezo, ife tikuyenera kuganiza chiyani mmawa uno, zitatha zaka naintini handiredi za kuwona kuvutika ndi mazunzo ndi zina zotero; kumadziwa kuti ife tiri pa khomo kumene lapatsogolo la chiukitsiro. Ameni. Mpingo wasunthira mmwamba kufika ku ora tsopano limene chiukitsiro chikhoza kubwera nthawi iliyonse. Ndipo ine ndikuganiza chimene icho chiti chidzatanthauze kwa ife pa tsiku limenelo, okhulupirira, chimene icho chiti chidzatanthauze pa tsikulo.

² Ine ndikukhoza kuwona mmawa wolawirira umenewo pamene Marita ndi Mariya ankapita ku manda. Iwo anali akuyenda mmphepete mwa phiri utadutsa usiku. . . Taganizani za mtima wa mayi wosauka uyo. Mwana wake njira yonse, pamene iye anali. . . pamene Iye anabadwa, iwo ankati Iye anali Mwana wapathengo, kuti mwamtheradi Iye sanali wa Yosefe, ndipo—ndipo Iye anali, kapena, Iye anali wa Yosefe, ndipo iwo anali. . . Mwanayo anabadwa kunja kwa chikwati choyera. Iye anadutsa zonse zimenezo, ndipo a, zonse, “chinthu chokhudza mwana wako,” ndipo mmene Iye anakanidwira, ndi kunyozedwa, ndi kulavuliridwa, komabe Iye anali kudzinenera izo. Ndipo iye, mwinamwake, ndi mtima wake ukunjenjemera, anati, “Mulungu anandipatsa ine Mwana ameneyo, izo zatheka bwanji?” Kumuwona Iye uko mu ora lalikulu lovuta lija.

³ Iye anaganiza ndithudi, pamene iwo amapita kuti akamuveke chisoti cha minga pa mutu Wake, ndi kumumenya Iye mpaka Magazi kumawonekera pa nsana Pake, kumuvula Iye maliseche ndi zinthu zonse izi; iye ankaganiza kuti ndithudi mphindi iliyonse Iye aponyera mtanda umenewo pansi ndipo apotoloka, adzamenyetsa phazi Lake pansi (dziko lichita chivomezi ligwera mbali imodzi ndi imzake) ndipo anena Yemwe Iye anali. Koma Iye anali atafa uko, ngati wosauka, chigawenga chogonjetsedwa atapachikidwa pa mtanda.

⁴ Iye anali atafa mwamanyazi. Inu mumawona chithunzi ndithudi chokhala ndi nsalu atamuveka Iye, icho chinali cholakwika. Iwo anamuvula chovala chirichonse pa Iye, basi pa. . . ndipo anamuchititsa Iye manyazi kwa dziko ndi chirichonse chimene iwo akanakwanitsa, ndipo iwo anamukhomera Iye pa mtanda.

Ndipo pamenepo Iye anawoneka kuti anali atayima kusowa kuti achita chiyani. Ataima, dziko lapansi silinamufune Iye, Kumwamba sikukanamutenga Iye, Iye anali wochimwa. Oh

mai! Ngati inu mutangozindikira, tangoganizani, dziko lapansi silinamufune Mlengi wake. Kumwamba sikukanamulandira Iye chifukwa Iye anali ndi tchimo la dziko lapansi pa Iye. Iwo analibe nkomwe malo. . . mukukamba za malo oti abadwire, Iye analibe malo oti afere. Uko nkulondola. Dziko lapansi silinamufune Iye. Iwo anamukana, anati, “Chokani naye munthu ameneyo.” Kumwamba sikumamulandira Iye chifukwa Iye anali kale, Iye anali wochimwa.

⁵ Oh, ndi wotani—ndi Mpulumutsi wotani! Kubwera kuchokera ku Ulemelero ndi kudzakhala izo chifukwa cha ine. Anakanidwa kwambiri ndi Ake Omwe, kuti, “Iye anabwera kwa Ake Omwe, Ake Omwe sanamulandire Iye.” Iye, analibe malo oti angabadwireko, analibe malo oti akaferere. Kodi dziko linkafuna chiyani pa Iye? Iwo akanachita chiyani koma kumuponyera Iye mu gehena.

Koma panali Winawake Amene ankamukonda Iye. “Ine sindidzasiya solo Yake mu gehena, komanso sindidzalola Iye kuti awone chivundi.” Koma Iye anamuukitsa Iye mmanda, ndipo Iye anadzawuka mmawa wa Isitara, atagonjetsa. Aleluya! Anaphwasula msinga iliyonse ndi mantha aliwonse ndi chirichonse, anawukanso ndipo akuima wamoyo lero, kwa nthawizonse.

⁶ Kukhalapo Kwake kuli pano, Iye ali pa malo ano mmawa uno wa kupembedza. Iye amakumana paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi. Inu mukudziwa mtima wokondwa umene ine ndiri nawo, kudziwa kuti malonjezo omwewo amene Iye anapanga mu Baibulo, “Zinthu zimene Ine ndikuzichita, inunso mudzazichita. Ine ndidzakhala ndi inu mpaka kumathero a dziko lapansi.” Anthu osauka, okanidwa, onyozedwa a dziko lino akhoza kukhalabe ndi Kukhalapo Kwake ndi ife. Wamphamvuzonse, wopezeka ponseponse nthawizonse, wopezeka paliponse, wamphamvu zonse, paliponse nthawi zonse. Momwe Iye anakonzera njira yothawirapo, mu ora lililonse la mavuto. “Ndine Thandizo lopezekeratu mu nthawi ya mavuto,” Iye anatero.

⁷ Tsopano, mmawa uno Iye ali moyo. Iye ali nafe lero. Ife tikhoza kungokhala mpingo waung’ono lero, ife tikhoza kungokhala kachisi wamng’ono, wakale, wokwera mmwamba apa, wopanda zochuluka zoti nkumuyang’anapo; koma sipanakhalepo malo odzichepetsa kwambiri, kupatula amene Iye angabwere kwa iwo. Iye ali moyo lero pakati pa amoyo. Iye sanafe, koma Iye ali moyo. Ndipo Iye akukhala pakati pa amoyo.

⁸ Mzanga wochimwa, lero, ngati ndiwe wakufa mu tchimo ndi mphulupulu, bwanji osakhala moyo? Nchifukwa chiyani ukukhala mu imfa? Bwanji. . . iwe wapindula chiyani pokhala mu imfa? Bwanji osabwera ku moyo? Bwanji osakhala moyo

lero ndi Iye? ndipo ndi chiyembekezo chodala chachikulu ichi, kuti ngakhale imfa payokha, ikukulekanitsa kwa okondedwa ako, siingakhoze konse kudetsa kapena kuwononga kapena kutengapo chirichonse?

Ndi chiyembekezo chodala bwanji. Ndi chinthu chopambana bwanji chimene ife tiri nacho lero, chifukwa cha chiukitsiro Chake. Ndipo Iye ali moyo, ndipo ife tikukhala moyo ndi Iye, ndipo tsiku lina Iye adzabwera, ndipo ife tidzapita ndi Iye. Pakuti, anati, “Pitani mukawauze ophunzira Anga ndi Petro kuti Ine nditsogola kukalowa mu Galileya.”

⁹ Iye nthawizonse amapita patsogolo pathu kuti akapange njira. Pamene palibepo njira, Iye anati, “Ine ndine Njira. Ndine Chiukitsiro, Ndine Moyo.” Ndipo mulole, lero, pamene ife tasonkhana pano lero. . . Inu mumamukonda Iye?

Iye ali moyo, Iye ali moyo, Khristu Yesu ali moyo lero!
 Iye akuyenda nane, Iye akuyankhulana nane, pa njira yopapatiza ya moyo.
 Iye ali moyo, Iye ali moyo, kuti apereke chipulumutso!
 Mundifunse ine momwe ndikudziwira kuti Iye ali moyo;
 Iye akukhala moyo mkati mwa mtima wanga.

¹⁰ Kodi zimenezo si zodabwitsa? Ndi angati amene ali ndi chiyembekezo chodala ichi mmawa uno, kodi mungakweze dzanja lanu? Ndithudi. Kodi alipo wina pano alibe chiyembekezo, amene angati, “M’bale Mlaliki, mmawa uno, inu mwa osonkhana awa, mukudziwa kuti ine ndasonkhana ndi inu pano pa mmawa wa chiukitsirowu, ndipo komabe, palibepo Moyo wachisavundi ukupuma mkati mwanga, ndipo chiyembekezo ichi sichikukhala mkati mwa chifuwa changa. Ine ndikufuna kuti inu nonse mukandikumbukire ine lero mu pemphero kuti ichi chikhale chiukitsiro mwa ine, kuti solo yanga iwukitsidwire mu chiyembekezo chodabwitsa ichi podziwa kuti tsiku lina ine ndikuyenera kudzatsamira pilo yotsamira pakufa ndipo ndidzakaikidwa mmanda kwinakwake, mmanda, kapena uko mnyanja, kapena kulikonse kumene kudzakhale malo anga odzafera; koma ine ndikufuna ndidzakhale ndi chiyembekezo chimenecho. Ine ndikukweza dzanja langa ndi kukupemphani inu kuti mundipempherere ine”? Alipo munthuyo? Kodi mungakweze dzanja lanu amene mulibe. . . ? Ine ndikuganiza kuti inu nonse ndi Akhristu ndiye. Izo nzopambana. Tiyeni. . .

¹¹ Ine ndikukhulupirira lero, pambuyo pa kubwereranso, kubwerera, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu Wamphamvuzonse atumiza Ambuye Yesu pano pa nsanja iyi lero, ndipo atsimikizira kwa inu kudutsa mthunzi wa kukaikira

kuti Yesu ali moyo ndipo ali pakati pa anthu lero. Amen. Ine ndikudziwa kuti Iye ali pomwe pano tsopano. Amen. Iye ali pano. Iye akukhala moyo. Iye tikumuwona Iye. Iye... Iye anati kwa Tomasi, “Mphotho yawo ndi yaikulu bwanji amene sanandiwonepo Ine ndipo komabe akukhoza kukhulupirira.” Amen. Iye ndi wodabwitsa.

¹² Tsopano, tiyeni tiimbe iyi. Tipatseni ife poyambira, Mlango Gertie, pa imeneyo, *Iye akukhala Moyo*. Ine ndikungokonda kuimva iyo ikuimbidwa mmawa uno. Oh, ife tikuwona zisoni ndi zosautsa ndi chimene mtengo wake unali, koma tsopano, tangoganizani, izo ziri paliponse. Aleluya. Kuwala kwa masana kwabwera. Sheol wathedwa. Hade kulibenso. Imfa yangokhala chowopsyezera. Mdima wonse wazimirira. Iye tikukhala moyo. Amen. Iye tikukhala moyo ndipo Iye ali moyo. Iye ali moyo, ndipo ife tikukhala moyo mwa Iye. Amen. Tonse pamodzi tsopano:

Iye ali moyo, Iye ali moyo, Khristu Yesu ali moyo lero!

Ndipo Iye akuyenda nane ndipo Iye akuyankhula nane panjira yopapatiza ya moyo.

Iye ali moyo, Iye ali moyo, kuti apereke chipulumutso!

Inu mukufunsa... momwe ndikudziwira... (Bwerani tsopano.)

Iye akukhala moyo mkati mwa mtima wanga.

Aliyense, mofuula mmene mungathere tsopano.

Iye ali moyo, Iye ali moyo, Khristu Yesu ali moyo lero!

Ndipo Iye akuyenda nane, Iye akuyankhula nane pa njira yopapatiza ya moyo.

Iye ali moyo, Iye ali moyo, kuti apereke chipulumutso!

Inu mukundifunsa kuti ndikudziwa bwanji Iye... (Kwezani dzanja lanu mmwamba tsopano.)

Iye akukhala moyo mkati mwa mtima wanga.

¹³ Gwiranani chanza ndi winawake wakhala pafupi ndi inu ndipo munene kuti, “Alemekezeke Ambuye.” Nonse ndinu Akhristu. Ndinu mzika limodzi. Oh, mai. Kodi zimenezo sizikukupangani inu kumverera bwino? Zakale zonse zaiwalidwa, izo zonse zatha. Ndani anachita izo? Iye ali moyo, Iye anachita izo. Ndani anachita? Khristu. Tiyeni tiimbe iyo kenanso, tsopano, mokweza mawu.

Iye ali moyo, Iye ali moyo, Khristu Yesu ali moyo lero! (Mantha onse anapita!)

...ndi ine ndipo Iye amayankhula nane
 poyenda panjira yopapatiza ya moyo.
 Iye ali moyo, Iye ali moyo, akupereka
 chipulumutso!
 Inu mukundifunsa ine momwe
 ndikudziwira . . . (Walani tsopano.)
 Iye akukhala moyo mkati mwa mtima wanga.

14 Oh, mai. Kodi izo si zodabwitsa? Mwanjiraina, imzake, iyo ikumveka mwapadera mmawa uno kwa ine. Mawu anu onse akugwirizana pamodzi, akumveka mokongola kwambiri. Kodi inu munazindikira izo? Zikungowoneka kuti izo zikuchokera pansu pa mtima wanu.

15 Zosamalira zakale zapita tsopano. Chiukitsiro chatsimikiziridwa. Yesu wauka kwa akufa, ndipo Iye akukhala moyo, ndipo ine ndikukhala moyo ndi Iye. Amen. Iye akumawonekera kwa ife, ndipo akuyankhulana nafe pa njirayi; akumatiwoneka ife masomphenya, zinthu zimene zinapita, ndi zinthu zimene ziri nkudza. Iye akumachiza matenda athu ndipo Iye akumatipatsa ife chimwemwe. Iye akumatipatsa ife mtendere. Ndipo pamene imfa iyang'ana pa nkhope, ife timakuwa, "Ine sindidzawopa choipa, pakuti Inu muli ndi ine." Momwe ine ndikuzikondera zimenezo! "Oh, imfa, mbola yako ilikuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Ine ndikupita kuchoka ku chigonjetso kupita ku chigonjetso." Kodi imfa ndi chigonjetso? Mwamtheradi, imfa ndi chigonjetso. Amen. Imfa ndi chigonjetso tsopano, osati chisoni. Ndi choncho, chabwino, ndi chigonjetso. Amen. Ine ndati . . .

16 Paulo anati, "Kusiya zinthu zimenezo mmbuyo, ine ndikulimbanira kufika pa malo a kuitana kwapamwamba." Amen. Pamene iwo anali kukonzekera kuti akamudule mutu wake, ndipo anadulidwa mutu uko ku Roma, iye anati, "Ine ndamenya nkondo yabwino, ndamaliza ntchito, ine ndasunga Chikhulupiriro: Kuyambira pano paikidwa kwa ine a—korona wa chirungamo, Ambuye, Woweruza wolungama, adzandipatsa ine pa kuwonekera Kwake: osati ine ndekha, koma onse amene amakonda kuwonekera Kwake."


17 Inu mungakonde mutamuwona Iye atabwera lero? [Osonkhana akuti, "Inde."—Mkonzi]. Inu mungakonde mutamuwona Iye? Ndipo pamene ife tikumana naye Iye mu mtendere, tangoganizani, titaima pamenepo, matupi akale oyipa awa. Mwina . . . iwo akhoza kukhala aang'ono ndi achinyamata, koma iwo adzakalamba. Tsitsi la imvi ndi a . . . ndipo mano ogweruka, ndi maso osawona bwino, mapewa akugwa. Koma basi kuseri kwa chophimba ichi apa, kumeneko kukuima mwamuna watsopano. Pamene msasa wa pansu pano udzapasuka, ife tidzakalowa mu watsopano, monga *choncho*. [M'bale Branham akukhwatchitsa zala zake—Mkonzi].

Ndithudi. Pakuti, Iye ali moyo; ife tiri moyo, nafenso. Ndipo ife tikukhala moyo mu chiyembekezo chodala ichi.

¹⁸ Ngati Iye atatenga nkhope zathu mmawa uno, ndi kukokera chophimbacho mmbuyo ndi kutiwonetsa ife, icho sichingakhale chikhulupiriro aponso, ndiye. Ife tingokhulupirira izo tsopano. Ndipo ife tikuzimverera, kuchokera ku Dziko linalo, kuphokosera kwa Ulemerero kukusunthiranso mmiyoyo yathu, kumawonetsera, “Izo nzoona! Izo nzoona! Kukankhira ku malo a kuyitana kwapamwamba!” Ndi nthawi yopambana bwanji! Ameni. Oh, Iye ndi weniweni kwambiri!

¹⁹ Tsopano, amzanga, ndi nthawi pafupifupi yoti titseke misonkhano. Ndipo ife tikufuna kuti inu mukadye kadzutsa wanu, mubwerenso tsopano ku—kudzapitiriza msonkhano. Ine ndigunda malire a izo lero, ine ndidzatero. . . ndi kugunda chiukitsiro. Koma mmawa uno, mu pafupifupi maora angapo; ndikufuna ndipite kunyumba ndi kukadzitsekera ndekha ku pemphero tsopano, pakuti ine—ine ndikupemphera kuti Mulungu atipatse ife weniweni, mzere wapemphero weniweni lero. Ndipo—ndipo kenako ine ndikufuna ndidzalalikire, pakapita kanthawi, pafupifupi maora angapo kuyambira pano, pa kukwera mmwamba, chimene Iye anachita pamene Iye ankapita mmwamba. Ife tawona chimene Iye anachita kuno ndi mtengo, tsopano ife tikufuna tidzawone zimene Iye anachita pamene Iye anapita mmwamba, ndi chimene Mulungu anachita pomugwiritsa Iye ntchito, ndi chimene Iye ali lero.

²⁰ Ambuye akudalitseni inu, ndiro pemphero langa. Aliyense akumverera chiukitsiro? Kodi inu mukungomverera chiukitsiro mu mtima mwanu?

²¹ Chabwino. Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa pemphero. M’bale Neville, ndikudabwa ngati inu mungatibalalitse ife, mu liwu la pemphero, ngati inu mungatero, pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. 

KUTULUKA DZUWA KWA ISITARA CHA56-0401s
(Easter Sunrise)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi pa Lamlungu la Isitara pa kutuluka kwa dzuwa, Epulo 1, 1956, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org